Kucimwa

Kwa Adamu

Paciyambi Mulungu adalenga Kumwamba ndi Dziko, ndipo adalenga Munthu m'cifanizo cace namucha dzina lace kuti Adamu.[1] Analibe ucimo ndiponso anali ndi cibwenzi cabwino ndi Mulungu.[2] Ndipo Yehova Mulungu ana muuza Adamu nati, m'tengo wakudziwitsa zabwino ndi zoipa usadye umenewo.[3] Koma Adamu ndi Mkazi wace sananve Mulungu ndipo anankhala Antu aucimo ogawanisidwa kwa Yehova.[4] Monga ucimo unalowa m'dziko lapansi mwa munthu M'modzi, ndi imfa mwa ucimo, cotero imfa inafikira anthu onse cifukwa kuti onse anacimwa.[5] Pakuti kulibe wolungama pansi pano amene acita zabwino osacimwa.[6] Malipilo aucimo ndi imfa, moyo wocimwawo ndiwo udzafa.[7]

Tonsefe tili ana a Adamu, pakuti Mulungu ana lenga mitundu yonse kukhala amwazi umodzi.[8] Kodi ndiciyani timangozipa? Kodi ndiciyani timazondana ndi acibale atu? Kodi mutima wa munthu waucimo unga tembenuke bwanji kuti ankhale ndi cibwenzi ca bwino ndi Mulungu? Mulungu anapatsa nsembe mumalo mwa Adamu kuti isuke ucimo lace.[9] Mulungu adzadzifunira yekha Mwana wa nkhosa wa nsembe yopsereza.[10] Adamu anaudza ana ace kuti Mulungu amafuna nsembe kuti ucimo wa munthu usukidwe. Munthu ayenera khupereka nsembe yolungama kuti ife mumalo mwa munthu. Abeli ana khulupirira Mulungu, ndipo mwacikhulupiriro anapatsa mwana wa nkhosa woyamba kuti ankhale nsembe ya ucimo wace.[11] Yehova anayanganira Abeli ndi nsembe yace.[12] Koma Kaini sana khulupirire Yehova. Anapatsa cipaso canchito zace zabwino. Mulungu sazayanganira nsembe imene ipatsidwa kucokera ku ubwino wathu.[13] Zolungama zathu zonse ziri ngati cobvala codetsedwa.[14] Kopanda kukhetsa mwazi kulibe kumasuka.[15]

Kodi Upembedzo Ulimbwanji? Upembedzo onse uma satira njila imodzi yamacitidwe abwino. A Hindu amapatsa nsembe, ama pempera, ndipo amankhala umoyo wa bwino; A Muslim amasata malamulo musanu

aci Islam; A Budda amakonka njira zili 8 za upembedzo wawo; Akatorika amapembedza kwa Maria, ndikulapira ucimowawo kwa M'kulu Wansembe, amadya mugonero ndiku patsa cuma kuti citandidze okondedwa awo amene anafa kuti afike kumwamba. Asabata ayetsetsa ku satira malamulo kumi amu buku lopaturika; ndipo ena ama khulupirira kuti ubadidzo umasuka ucimo, pakuti pakusadziwa cilungamo ca Mulungu, ndipo pofuna kukhazikitsa cilungamo caiwo okha, iwo sanangonja ku cilungamo ca Mulungu.[16] Upembedzo onse udza kuperekani kumalo amodzi, kukaniwa ndi Mulungu, kuponyedwa mu Gehena.[17] Kodi ndiciyani timapa abale athu? Cifukwa tili aupembedzo wa Kaini amene anali mwana wawoipayo (Satana) ndipo anapa m'bale wace. Ndiciyani anamupa? Cifukwa macitidwe ace anali woipa koma ambale wace anali abwino[18]

Ino ninzi tulajayana? Nkaambo bukombi bwesu mbubwa Kaini, walo waali wa-mubi (Saatani) wakajaya munyina. Ninzi ncaka mujaila? Nkaambo incito zyamunyina zyaali zibotu izyakwe zyaali sofweede.[19] Ndi cikhulupiriro Abeli anapereka kwa Mulungu nsembe yoposa ija ya Kaini, imene anacitidwa umboni nayo kuti anali wolungama; nacitapo umboni Mulungu pa mitulo yace; ndipo momwemo iye; angakhale adafa alankhulabe.[20]

Yesu Kristu Ndani? Mulungu anapereka nsembe yace ya ucimo pakuti Mulungu anakonda dziko lapansi kotero kuti anapatsa Mwana wace wobadwa yekha kuti yense wakukhulupirira iye asatayike koma akhale nao moyo wosatha.[21] Kuti Kristu anafera zoipa zathu, ndi kuti anaikidwa m'manda, ndi kuti anaukitsidwa tsiku lacitatu.[22] Kodi ana kwanitsa bwanji? Ni Mulungu!! Paciyambi panali Mau, ndipo Mau anali kwa Mulungu ndipo mau ndiye Mulungu.[23] Ndipo Mau anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife.[24] Koma Iye m'mene adapereka nsembe imodzi, cifukwa ca macimo, anakhala pa dzanja lamanja la Mulungu cikhalire.[25] Tayeretsedwa mwa

copereka ca thupi la Yesu Kristu kamodzi kwatha.[26] Koma onse amene anamlandira iye, kwa iwo anapatsa mphanvu yakukhala ana a Mulungu, kwa iwotu aku khulupirira dzina lace.[27] Kodi ndinga mulandire Motani? Utembenuke ku ucimo wako, kuti ngati udzabvomereza m'kamwa mwako Yesu ndiye Ambuye, ndi kukhulupirira mumtima mwako kuti Mulungu ana muukitsa kwa akufa, udzapulumuka.[28] Mulungu anapatsa nsembe imodzi cabe ya macimo kwa anthu amitundu yonse, ndipo ngati ife mwa cikhulupiriro ta mu landira, tidza pastidwa mpaso yaulele ya umoyo osata. Upempere kwa Mulungu, kupempa kuti akululukire macimo ako ndipo ulandire nsembe (Yesu) lero.

Cifukwa cace ngati munthu ali yense ali mwa Kristu ni wolengedwa watsopano; Zinthu zakale zapita, taonani zakhala zatsopano.[29] Taonani ndaima pakhomo (mutima wako) ndigogota, wina akamva mau anga nakatsegula pakhomo, ndidzalowa kwaiye, ndipo ndidzadya naye, ndi iye ndi ine.[30]

Ndime; (1) Genesis 1:1 (2) Gen 1:27 (3) Gen 2:19 (4) Gen 2:17 (5) Gen 3:24 (6) Aroma 5:12 (7) Mlaliki 7:20 (8) Ezek 18:20 (9) Macitidwe 17:26 (10) Gen 3:21 (11) Gen 22:11 (12) Gen 4:4 (13) Gen 4:3,5 (14) Isaya 64:6 (15) Ahebri 9:22 (16) Aroma 10:3 (17) Miyambo 14:12 (18) Cibvumb 21:8 (19) 1 Yohane 3:12 (20) Ahebri 11:4 (21) Yohane 3:16 (22) 1 Akorinto 15:3,4 (23) Yohane 1:1 (24) Yohane 1:14 (25) Ahebri 10:12 (26) Ahebri 10:10 (27) Yohane 1:12 (28) Aroma 10:9,10 (29) 2 Akorinto 5:17 (30) Cibvumbu 3:20

Conde ngati mwankhala muli kulandira nsembe ya Mulungu Yesu Kristu, conde Lemberani ku Keyala (mu Africa)

FELLOWSHIP TRACT LEAGUE
P.O. BOX 164 • LEBANON, OH 45036
www.fellowshiptractleague.org © Tract 8078 (Chichewa)
All tracts free as the Lord provides. Not to be sold.